# KODI MAPWANDO ANAKHOMEREDWA PA MTANDA KAPENA AYI?

Cholinga cha phunziroli ndichofuna kufufuza kuchokera m'baibulo komanso m'mabuku amzimu wachinenero kut,i kodi maphwando amene Mulungu analamulira kwa ana Aisrayeli ndiofunikabe mpaka lero kapena anakhomedwa pamtanda?

Poyamba tiyen tione mu buku la mlongo **Ellen G. White**

Mu **Testmonies to the Ministers 437.1** Mulungu Sadzawatsutsa anthu pachiweruzo pachifukwa choti mokhulupirika anakhulupirira bodza; koma pachifukwa choti ananyalanyadza mwai wozipanga okha kulunjika ku chowonadi.Opusa sadzatsusidwa chifukwa chopusa koma chifukwa choti sanatengele mwai ndi kuthekera komwe Mulungu anawapatsa kuti akafikire kuti akhale mkhristu.

Kuli zinthu zambiri zomwe anthu anakhulupira ngati zoona koma zowona zake Zikhulupiro zimenezi sizovomerezeka ndi mau a Mulungu. Pokha pokha ngat anthuo sanafufuza kuti zomwe akukhulupirazo ndi zolakwika ,Mulungu sazawa weluza iwo chifkwa cha ichi.

**TINGAZIWE BWANJI CHIMENE MULUNGU AMAYEMBEKEZERA IFE KUTI TIKHULUPIRE KOMANSO KUMAZICHITA,KUTI TIKAKHALE ANGWIRO PAMASO PAKE?**

Tiyeni tione zomwe Mulungu analamulira makolo athu oyamba kuti azichita .**Deuntronomo 6:1 -2,17**

Kuchokera mu ves **1-2** ; Tapeza kuti Mulungu akupereka kwa ana a Israyeli

***1-Malamulo***

***2-Malemba***

***3-Maweruzo***

Izizi zimayenera kusungidwa kupyorera moyo wawo wonse.

Mu Vesi 17; Tikuonanso kuti akufusidwanso kusunga **Maumboni** kuonjezera pa malamulo ali pamwambawa.

***Choncho tikupeza kuti zonse zimene Mulungu akuwalamula kuti a Israyeli azisunga ndi :***

***1-Malamulo {malamulo khumi Eksodo 20:3-17}***

*2-malemba {maphwando{,Masalimo 81:1-3 }*

*3-Maweruzo {malamulo apachikhalidwe Levitiko 18: 1-30}*

*4-Maumboni {Yesaya 8:20.}*

## CHIFUKWA CHANI AMAYENERA KUSUNGA MALAMULO ANAYI AMENEWA

**Deuntronomo 6:24-25**

Kuchokera m'mavesiwa tapeza zifukwa zomwe amayenera kusungira malamulo anayi aja. Zomwe ndi:

*1.Kuti aope Mulungu,*

*2.Kuti alandire madalitso,*

*3.Kuti alandire chitetezo,*

*4.Kuti alandire chizindikiro cha chilungamo,*

## CHIFUKWA CHA KUCHIMWA NDI CHANI CHOMWE MULUNGU AKUONJEDZERAPO PAMBALI PA MALAMULO ANAI AJA?

**Numeri 19:1-2,**

Lamulo lopereka nsembe ya nyama linaonjezedzeredwa, kwa iwo linali chithuzithuzi cha thupi la Yesu Khristu,amene amaynera kubwera kudzafa pa imfa ya Pamtanda.

Chocho ana a Israyeli anakhala akupha nyama ,monga nsembe kufikira pamene Yesu anabwera kudzafa pa imfa ya pamtanda.

Apa tsono tikupedza kuti tsopano pali malamulo okwana asanu omwe ndi :

*1.Malamulo,*

*2.Malemba,*

*3.Maweruzo*

*4.Maumboni*

*5.Kupereka kwa zinsembe*

## YESU ATABWERA ANACHITA CHANI NDI LAMULO LA ZINSEMBE?

Yesu atabwera anakwanilitsa ena Mwamalamulowa.Chocho pofuna kusiya kusatila /kuchita lina lililonse la mwa Malamulowa; Baibulo likuyenera kutiuza kuti ndi liti mwa

malamulo amenewa  linakhomedwa pamtanda ; kapena kuti linakwnilitsidwa pa imfa ya Yesu Khristu pamtanda.

Ngati ndi malamulo khumi; Baibulo likuyenera kufotifotokozera ngatinso ndi Malemba, Maweruzo ,Maumboni,kapena Zinsmbe za nyama; Baibulo likuyeneranso kutiuza. Ngati Baibulo silikufotokodza kanthu pamenepo , tidzaweruzidwa chifukwa chosasunga malamulo  amene tinalamulilidwa kuwatsunga.

## KODI MTUMWI PAULO AKUTNJI MU AKOLOSE 2:14;

Apa baibulo likuti lamulo la zinsembe {ordinance} kupereka nsembe ya nyama linachotsedwa ndipo linakhomeredwa pamtanda.

Vesili silikuti Malamulo,kapena Malemba kapena Maweruzo kapena Maumboni  kuti anakhomedwa pa mtanda ayi mpang'ono pomwe; koma Lamulo la Zinsembe, ndilomwe linakhomeredwa pamtanda.

## CHIFUKWA CHIYANI LINAKHOMEDWA PAMTANDA

Chifukwa choyamba lina chotsutsana ndi Ife, chifukwa limakhuza kupha kwa nyama , pamene Mulungu analamulira kuti Tisaphe kumalamulo khumi.

Apa zingatheke bwanji kumasunga lamulo loti tisaphe panthawi yomweyo tikumapha nyamba? ***Yesaya 66:3.***

Paulo yemweyo akupitiliza kufotokoza mu **Akolose 2:16-17**-Akuti "Chifukwa chake munthu asakuweruzeni mchakudya kapkena mchakumwa kapena mkulemekedza tsiku la phwando kapna tsiku la kukhala mwezi kapena la Sabata ndizo mthunzi wa zilikudzadzo koma thupi mla Kristu.

Chifukwa cha ichi mukapezeka mukusunga mipumulo kapena tsiku la kukhala mwezi ndi la sabata munthu aliyense askuweruzen inu kuti muziphanso nyama mmatsiku amenewa.

Pakut zolembedwa za zinsembe za nyama zinachosedwa ndikukhomeredwa pa mtanda; koma zithu izi : Ma Sabata ,kukhala kwa mwezi ndi matsiku ena opuma ndidzo mthunzi wa dzilikudzadzo koma thupi la Khristu ndilomwe limayimirilidwa ndi nyama zomwe zimaperekedwa msembe, ndipo ili ndi thupi lomwe linakhomeredwa pa mtanda.

Ndipo ngati Sabata,kukhala kwa Mwezi ndi mipumulo ina zinalibe mthudzi wa zinthu zirikudza munthawi ya Paulo, utadusa mtanda ndiye kuti tikuyenera kupitiridza kumasungabe kufikila zitakwanilitsidwa zoyimilila dzeni dzenizo.

Pamenepa baibulo silinationetse kuti masiku amenewa kapena kuti malamulo onse anakhomedwa pamtanda; kupatula lamulo la zinsembe lokha ndilomwe tapedza kuti linakhomedwa pa mtanda, chocho sitikuyenera kuwachotsa, tikuyenerabe kuwasunga

iwo pa zifukwa zofanana zomwe ana a Israyeli anayenera kusungira malamulowa monga taona kale mu buku la ***Deuntronomo 6:24-25;***

Kuti ***:1 –Tiope Mulungu***

***2.-Tilandile Madalitso***

***3-Tilandile chitetedzo***

***4-Tilandile chizindikiro cha chilungamo***

Ndithudi tikusowekadi madalitso amenewa pamene Dziko likuipiraipirabe.

## NDI CHANI CHOMWE MULUNGU AKUCHITA POFUNA KUTIKUMBUTSA IFE KUFUNIKA KOTSUNGA MALAMULO AMENEWA

Pachifukwa ichi Mulungu akutilonjedza kudzera mwa m'neneri, :

***Malaki 4:4-6; 4 "Kumbukilani chilamulo cha Mose mtumiki wanga, ndinamlamuliracho m'Horebu chikhale cha Israyeli lonse, ndicho malemba ndi maweruzo. 5-Taonani, ndidzakutumizirani Eliya mneneri lisanadze tsiku lalikuru ndi loopsa la Yehova. 6-Ndipo adzabwezera mitima ya atate kwa ana,ndi mitima ya ana kwa atate awo; kuti ndtsafike ndi kukantha dziko lionongeke konse."*** Akutitumidzira Eliya m'Neneri litsadze tsiku lalikulu loopsa la Ambuye kuti abwedzeretse Malamulo omwe dziko likuta anakhomedwa pa mtanda.

***Nehemiya 9:13-14; 13-Munatsikiranso pa phiri la Sinai, nimunalankhula nao mochokera m'mwamba, ndipo munawapatsa maweruzo oyenera, ndi chilamulo chowona, malemba , ndi malamulo okoma; 14-Ndi Sabata lanu lopatulika munawadzitsa, nimunawalamulira malamulo, ndi malemba, ndi chilamulo, mwa dzanja la Mose mtumiki wanu.***

## KODI NDI DZITHU ZITI ZOMWE ELIYA WOLONJEZEDWA ADZABWEZERETSE

Tiyeni tsopano tione zinthu zomwe mneneri wolonjezedzedwa akubwezeretsa.

***Maslimo 81:3-4 Ombani lipenga pokhala mwez, utakula mwezi , tsiku la phwando lathu .4.Pakuti ichi ndi cholemba cha kwa Israyerli ,; Chiweruzo cha Mulunguwa Yakobo***.

Kuchokera mu vesili, taphunzira kuti tsiku lomwe Mwezi wakhala (kapena kuti waoneka kumwamba) ndi tsiku la pwando ndilo lemba. {**Malaki 4:4-5;**}

Ichi ndichifukwa chake tikunva za kusunga kwa ma Phwando m'masiku ano omaliza.

Pakuti Mulungu analonjeza kuti Yesu asanabweranso kachiwiri, adzatitumidzira Eliya m'neneri kudzatiuza Ife kapena kuti kutikumbutsa za kusunga Malemba ,Maweruzo

komanso Maumboni, pakuti izi ndi zomwe dziko lapondereza. Mwa Malamulo anai awa:

***-Malamulo khumi***

***-Malemba,***

***-Maweruzo,***

***-Maumboni**,*

Zachidziwikire kuti lero anthu omwe akuti akuyembekedzera kubwera kwa Yesu khristu kachiwiri akungosungako zithu ziwiri basi ; zomwe ndi **Malamulo khumi** komanso **Maumboni**.

Koma Mulungu akufuna kuti tidzisunga zonse kuphatikidzapo **Malemba** ndiponso **Maweruzo** ngati tikufuna kuti tisindikidzidwe Chizindikiro chake.

***Yakobo 2:10***; akuti ***:Pakuti amene ali yense angasunge malamulo onse, koma akakhumudwa pa lomodzi, lyeyu wachimwira onse.***

Ndichifukwa chake Mulungu akutitumidzira Eliya m'neneri osat wa ku Tisibe,koma wokhala ndi mzimu komanso mphavu monga ya Eliya wa ku Tisibe, kudzabwezeretsa malo Ogamuka.

**Patriarchs Prophets.678.2**; **Munthawi yakumapeto gawo lina lililonse lopatulikira Mulungu lidzabwezeretsedwanso ; magawo omwe anachotsedwa munthawi yomwe Sabata lina sinthidwa ndi Munthu akuyenera kubwedzeretsedwanso;. Mulungu ali ndi anthu Otsala oima pa maso pa Dziko monga okonzanso ,akuyenera kuonenesera kuti Lamulo la Mulungu ndi maziko azonse**…………………………..

## NDI NDANI AKUCHITIRA UMBONI PA NKHANI IMENEYI

***Nahumu 1:15***; ***Taonani pamapiri mapadzi a iye wakulalikira uthenga wabwino, wakubukitsa mtendere! Chita madyerelo ako, Yuda kwaniritsa zowinda***;…….

### NDIPATI M'BAIBULO PAMENE TIKUPEZA NKHANI ZOKHUDZA MAPWANDO AMENEWA?

Tikamawerenga baibulo mu maka mu buku la **Levitiko 23:1-33**, akufotoza za ma phwando amenewa komanso ndi nthawi yake paja Mulungu wathu ndi wa dongosolo komanso wanthawi.

## UMBONI KUCHOKERA MZIMU WACHINENERO UKUTINJI?

**RH.May 6, 1875,Khristu anapereka kwa Mose, malangizo achipembezo kuti akawatsogolele m'moyo wao wa tsiku ndi tsikiu; ma phwano anidwa kuti akatetezere malamulo khumi ; Sanali mthunzi wodzatha pa imfa yake ya pa mtanda.**

**AMBUYE AKUDALITSENI CHIFUKWA CHOWERENGA UTHENGAWU.**

**NGATI MUKUFUNA KUMVA ZAMBIRI TIPEZENI PA MASAMBA A INTANETI AWA: Facebook@BSM TV /YouTube@ BSM TV KAPENA PA MANAMBALA AWA:**

# -0883714187/0994321446

# -0881764072/0992336738